

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

MUYAMBE MWAFUNA

Moyo ndi wodzaza ndi zisankho za tsiku ndi tsiku. Kodi nditani? Ndipite kuti? Kodi ndinene chiyani? Ndizichita bwanji? Kodi ndizigwiritsa bwanji nthawi yanga, mphamvu zanga komanso ndalama zanga? Mitima yeniyeni ya anthu imaonekera kudzera mu zisankho zomwe amapanga, mosasamala kanthu za zomwe anganene kapena kuonetsera. Zisankho zao zimasonyeza zimene amaika patsogolo m'moyo wao. Anthu a dziko amafunafuna zosangalatsa, ndalama, kutchuka, kumasuka, ndi zina zotero. Yesu anaphunzitsa mu Chiphunzitsa cha pa Phiri kuti “koma muyambe mwafuna Ufumu wa Mulungu, ndi chilungamo chake” (Mateyu 6:33).

Kuika zinthu za Mulungu patsogolo kuyenera kukhala chinthu chofunika kwambiri kuposa china chilichonse. N'zomvetsa chisoni kuti pali anthu ambiri amene amatchula dzina la Khristu koma akuyesetsa kuchita zinthu za dzikoli, ndipo kwa iwo zinthu za Mulungu sizofunika kwambiri. Miyoyo ya Akhristu iyenera kufotokozedwa ndikuzindikirika malingana ndi mmene amamutsatirira Khristu ndi chilungamo chake.

Pali zinthu zofunika zomwe tonsefe tiyenera kuzisamalira m'moyo. Timafunikira chakudya ndi zovala, ndipo m'pofunikanso kukhala ndi nthawi yocheza ndi banja lathu, kugona ndi kugwira ntchito. Asanaphunzitse za kufunafuna Ufumu wa Mulungu, choyambirira Yesu anavomereza za zosoweka zimenezi. “Chifukwa chake musadere nkhawa, ndi kuti, Tidzadya chiyani? Kapena, Tidzamwa chiyani? Kapena, Tidzavala chiyani? Pakuti anthu akunja azifunitsa zonse zimenezo; pakuti Atate wanu wa Kumwamba adziwa kuti musowa zonse zimenezo” (Mateyu 6:31-32). Yesu sanali kuphunzitsa kuti tizinyalanyaza zinthu zimenezi, koma anali kuphunzitsa kuti tisamade nazo nkhawa chifukwa Mulungu

amadziwa zosowa zathu ndipo adzatipatsa zosowa zathu. Iye ankaitana otsatira ake kuti aziika Mulungu patsogolo ndi kuika zinthu za Yehova pamwamba pa china chilichonse. Iye analonjeza kuti zinthu zina zonsezi “zidzaonjezedwa kwa inu” (Mateyu 6:33b).

Kuti Mkhristu apeze chimwemwe ndiponso chenicheni cha chipambano potumikira Mulungu, zinthu za Mulungu ziyenera kukhala zoyambirira. Palibe cholakwika kukhala ndi maloto, zolinga, malingaliro ndi zokhumba koma zinthu zonsezi ziyenera kuperekedwa kwa Mulungu ndipo nthawi zina kuziika pambali kapena kuzichedwetsa pofuna kuti Mulungu akhale woyamba. Palibe chinthu china chofunika kwambiri kuposa miyoyo yathu yamuyaya, ndipo tiyenera kuona kufunika kwa kusamalira miyoyo imeneyo pamwamba pa zinthu za dziko.

Pa chisankho chilichonse chimene tingachite, tiyenera kudzifunsa tokha kuti, “Kodi ndikuika Mulungu patsogolo?” Akhristu ambiri akhoza kudzilungamitsa ndiponso kukometsa zisankho zao popereka zifukwa zomwe Yesu mwini anazitchula mu Luka 14:16-20. Ena amafotokoza zifukwa zimene sadzipereker kapena kuikirapo mtima pa zinthu za Mulungu ndipo amati: Ndili ndi chuma chimene ndiyenera kupita kukachiyang'anira, ndili ndi ng'ombe zimene ndiyenera kuzisamalira, kapena ndangokwatira kumene. Mndandandawu ukupitirirabe, koma kodi Mulungu ndiye amene mumaiika patsogolo? Kodi zisankho zanu zikusonyeza zimenezo?

Zinthu zololedwa zimene sizili tchimo kawirikawiri zimatidyera nthawi ndi zomwe timazilabadira. Akhristu ayenera kuika Mulungu pamwamba pa zinthu zololedwazi, pakuti monga msampha, zosamalira za moyo zimenezi zikhoza kutsamwitsa chipatso

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Mitima yeniyeni ya anthu imaonekera kudzera mu zisankho zomwe amapanga, mosasamala kanthu za zomwe anganene kapena kuonetsera. Zisankho zao zimasonyeza zimene amaika patsogolo m'moyo wao.”

Muyambe Mwafuna

Mau a Mkonzi

Kalozera posanthula
Baibulo: Makiyi
Akhristu Atsopano

Makiyi kwa Akhristu
Atsopano

Kodi Mukudziwa?
Mau a Nyengo Yake:
Mulungu Adzamalza
Zimene Wyamba

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

chazimu ngati sitisamala. Yesu anati: “Koma mudziyang’anire nokha, kuti kapena mitima yanu ingalemetsedwe ndi madyaidya ndi ... zosamalira za moyo uno...ndi kuti tsiku ilo lingafikire inu modzidzimutsa ngati msampha pakuti lidzatero ndi kufikira anthu onse akukhala pankhope padziko lonse lapansi” (Luka 21:34-35).

Kodi tikufuna Mulungu poyambirira kapena tikuika patsogolo zinthu zololezeka? Tiyenera kufunafuna Mulungu choyamba ndi kumulola kuti atitsogolere kumene tikukhala, amene timakwatirana naye, ndi zimene timachita pa ntchito. Zinthu zololezekazo ziyenera kukhala zachiwiri. Anthu ambiri akufunafuna kuti choyamba chikhale chuma cha dziko lino. Ngakhale kuti sikulakwa kukhala ndi ndalama, n’kulakwa kulola kuti kufunafuna ndalama kukhale chinthu choyambirira ndipo Mulungu akhale wachiwiri.

Akhristu akafuna Ufumu wa Mulungu kukhala choyambirira, amamupatsa Mulungu zimene zili zabwino kwambiri, kuyambira nthawi yao, ndalama zao komanso luso lao. Tsiku lililonse, pamafunika kupeza nthawi yowerenga Baibulo ndi kupemphera. Ngati tinyalanyaza pa zimenezo, ndiye kuti pali china chimene tikuchitenga kukhala chofunika kwambiri. Pamene yakwana nthawi yopembedza ndi kuyanjana ndi oyera mtima, kodi timakhalapo? Kodi tikufuna Ufumu wa Mulungu kukhala choyamba? Kodi chikutenga malo oyamba ndi chiyani, pamene pali zinthu zofuna chuma mu ntchito ya Mulungu, komabe ife tikugwiritsa ntchito ndalama pa zinthu zokhudza ife tokha. Timasunga ndalama zakuti tidzagwiritse ntchito mtsogolo koma sitipereka chuma modzikhuthula?

Zinthu zimene Mkhristu weniweni amaika patsogolo zimakhala zosiyana kwambiri ndi za anthu akudziko. Paulo anaphunzitsa mpingo wa ku Roma kuti: “Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a panso pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuniro cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiwo” (Aroma 12:2). M’badwo uno ukusowa kukonzanso kwa malingaliro ao kuti umvetsetse zakuti kuyamba kufunafuna ufumu wa Mulungu ndiye chochitika chenicheni ndipo kumaposa kungonena zaumulungu. ■



OSAMUFUNSA
MUNTHU ZOMWE ZILI
ZOFUNIKA KWA IYE.
MUNGOONA MOMWE
IYE AMACHITIRA NDI
NTHAWI YAKE.

-Dale Carnegie

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m’dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Koma ndi kuchita zoona mwa chikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira Iye amene ali mutu ndiye Khristu. —Aefeso 4:15

Ndizosangalatsa kuona moyo utasinthidwa ndi Yesu. Ndi chinthu chodabwitsa kukhala ndi makanda obadwa kumene muuzimu ali mu thupi la Khristu. Otembenuka atsopano amabweretsa moyo ndi chisangalato kwa anthu a Mulungu, ndipo chisamaliro chao ndi kupezeka kwao kumatsitsimutsa moyo wa kupembedza ndi chiyanjano. Komabe, cholinga chidzikhala chofuna kuonjezera makanda atsopano auzimu ndi kuti makanda okulirapo akule mwa Khristu. Ambuye amafuna kuti otembenuka mtima atsopano achite bwino mu uzimu ndi kukhala mizati mu mpingo wa Mulungu.

Ndizomvetsa chisoni kuti otembenuka atsopano ambiri amakhala m'zikhaliidwe zofooka komanso kuti imfa ya makanda amuzimu ndiyokwera kwambiri. Siziyenera kukhala choncho, popeza Mulungu anakonzeratu chakudya chonse chazimu ndi chisamaliro chakuti Akhristu atsopano akule moyenera. Ambiri mwa otembenuka mtima kumene amabwerera mmbuyo kapena amakula mokwinimbira. Akhristu atsopano sayenera kuopa kuti akanika kukhala ndi moyo wabwino potumikira Mulungu. Pali madalitso aakulu ndi zipambano kwa aliyense amene angatenge uphungu ndi kutsatira dongosolo la Mulungu.

Mtolo wa kalata ya ulendo uno ndiwo kugawana zina mwa mfundo zomwe Akhristu atsopano angawiritse ntchito kuti akhalebe ndi moyo ndikukula mwauzimu. Ngakhale kuti cholinga cha kalatayi chili pa otembenuka mtima kumene, kugwiritsa ntchito mfundozi tsiku ndi tsiku kumapangitsanso Akhristu okhwima kale kukula ndi kupita patsogolo. Mulungu adzachita mbali yake kuti tipambane, koma ifeyo sitingakhale pansu ndi kupinda manja. Tiyenera kukhala okhulupirika ndi kusankha zochita mwanzeru kuti cholinga cha Mulungu chikwaniritsidwe mwa ife. Tiyenera kupangitsa kuti ubale wathu ndi Mulungu kukhala chinthu choyambirira ndi kutsatira molimbika zinthu za Ambuye.

Wotembenuka watsopano sayenera kuthedwa nzeru ndi zosowa zauzimu, pakuti chipulumutso ndi ulendo wa tsiku ndi tsiku—pang'ono ndi pang'ono. Mulungu adzatipatsa mphamvu ndi kutithandiza tsiku ndi tsiku pamene tikufunafuna chifuniro chake m'miyoyo yathu. Mukafika pachiteseko chokhoma, mumayang'ana makiyi anu ndikupeza kiyi woyenera. Pali makiyi ambiri auzimu omwe tili nao ngati tichita khama ndi kuwagwiritsa ntchitoyi moyenera.

Ngati mwangopulumutsidwa kumene, limbikitsidwani. Ambuye adzakuthandizani kukula, kubala zipatso, ndi kukhala ndi chipambano pamene muchita mbali yanu. “Khalani amphamvu, limbikani mitima, musamachita mantha, kapena kuopsedwa chifukwa cha iwowa; popeza Yehova Mulungu wanu ndiye amene amuka nanu; Iye sadzakusowani, kapena kukusiyani” (Deuteronomo 31:6). N'zoonadi kuti Yehova amakukondani kwambiri.

Ambuye akudalitseni ndikusungeni mu chisamaliro chake ndi chisomo.

Michael W. Smith

July 2023



LAPANI NDI KUBATIZIDWA (MACHITIDWE 2:38)

Atatha kupulumutsidwa, chimodzi mwazochitika zoyamba za kumvera ndi chakuti otembenuka mtima atsatre chitsanzo cha Yesu mu ubatizo wamadzi womiza kwathunthu. Ubatizo ndi umboni wa moyo woukitsidwa wa uzimu mwa Khristu ndipo ndi umboni wakunja wa chipulumutso. Baibulo limalangiza amene atembenuka kumene kuti abatizidwe pamene angopulumutsidwa.

Izi zimathandiza kulimbisa chochitika cha chipulumutso ndipo ndi njira yolimbana ndi kukaikira kuchokera kwa mdani. Ngati mwapulumutsidwa ndipo simunabatizidwe, ndikukulimbikitsani kuti musachedwe.

Choonadi cha Uthenga Wabwino Kalata 10: Ubatizo



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.



Kalozera posanthula Baibulo

Mutu: Makiyi kwa Akhristu Atsopano

Kuwerenga Malemba: Chifukwa chake monga momwe munalandira Khristu Yesu Ambuye, muyende mwa Iye, ozika mizu ndi omangiririka mwa Iye, ndi okhazikika m'chikhulupiriro, monga munaphunzitsidwa, ndi kuchulukitsa chiyamiko. — Akolose 2:6-7

Mwachidule: Pali makiyi auzimu othandiza Akhristu atsopano ndi okhwima kale omwe angatsekule zitseko za kukula kuuzimu ndi kupambana. Pamene Akhristu atsopano agwiritsira ntchito makiyi amenewa, adzatha kukhala ndi moyo wosasinthasintho, waumulungu.

I. Khazikitsani cholinga chanu

- A. Akolose 3:1-2 Khalani ndi chikondi pa zinthu zakumwamba.
- B. 2 Akorinto 7:10-11 Kusamala, chikhumbo, changu.

II. Imani pa chikhulupiriro, osati pa zomvaimva

- A. 2 Akorinto 5:7 Muziyenda mwa chikhulupiriro osati mwa zooneka ndi maso.
- B. Aefeso 2:8-9 Chipulumutso ndi mphatso.
- C. Aroma 8:1 Palibe kutsutsidwa mwa Khristu.

III. Pangani ubale ndi Khristu

- A. Yohane 15:4-5 Khalani mwa Khristu.
- B. Marko 12:30 Uzikonda Mulungu ndi mtima wako wonse.

IV. Yendani mokondweretsa Mulungu tsiku lililonse

- A. Yohane 14:15 Sungani malamulo.
- B. Ahebri 12:14 Khalani ndi moyo wachiyero.
- C. 1 Akorinto 10:31 Chitani zonse ku ulemerero wa Mulungu.

V. Madalitso a chisomo

- A. 2 Petro 3:18 Kulani m'chisomo.
- B. Ahebri 4:16 Thandizo pa mpando wachifumu wachisomo.
- C. 2 Akorinto 12:9 Chisomo cha Mulungu nchokwanira.

VI. Chepetsani mayesero

- A. Mateyu 26:41 Musalowe m'kuyesedwa.
- B. Aroma 13:14 Musapereke mpata ku zinthu zathupi.

VII. Mukhalebe ndi chikumbumtima choyera

- A. Luka 19:8-9 Bwezerani zonse munaba kapena kuononga.
- B. Machitidwe 24:16 Khalani nacho chikumbumtima chopanda chokhumudwitsa.

VIII. Phunzirani Baibulo

- A. 1 Petro 2:2 Khumbani Mau.
- B. 2 Timoteo 2:15 Phunzirani mau a choonadi.
- C. 2 Timoteo 3:14-17 Pitirizani m'Malemba.
- D. Salmo 119:105 Baibulo limaunikira njira.

IX. Pempherani

- A. 1 Atesalonika 5:17 Pempherani kosalekeza.
- B. Afilipi 4:6 Zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu.
- C. 1 Petro 5:7 Kutula nkhwawa zanu zonse pa Mulungu.

X. Kuyanjana ndi okhulupirira ena

- A. Ahebri 10:25 Musaleke kusunkhana.
- B. Akolose 3:16 Kulimbikitsana wina ndi mnzake.

XI. Uzani ena za umboni wanu

- A. Chivumbulutso 12:11 Kugonjetsedwa ndi umboni wanu.
- B. Aroma 1:16 Musachite manyazi ndi Uthenga Wabwino.
- C. Marko 16:15 Lalikira uthenga wabwino.

XII. Gwirani ntchito Ambuye

- A. Aefeso 2:10 Yendani mu ntchito zabwino.
- B. Mateyu 6:19-20 Ikani chuma kumwamba.
- C. 1 Akorinto 14:12 Khalani achangu pa mphatso zauzimu.
- D. Yakobo 2:14-17 Chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa.

XIII. Muzionana zinthu zofunika kwambiri

- A. Mateyu 6:33 Muyambe mwafuna Ufumu wa Mulungu.
- B. Aroma 12:2 Musafanizidwe ndi makhalidwe a panso pano;

Kumaliza

Abale, ine sindiweregera ndekha kuti ndatha kuchigwira: koma chinthu chimodzi ndichichita; poiwaladi zam'mbuyo, ndi kutambalitsira zam'tsogolo, ndilonetsa polekezerapo, kutsatira mfupo wa maitanidwe akumwamba a Mulungu a mwa Khristu Yesu. — Afilipi 3:13-14

MAKIYI KWA AKHRISTU AT SOPANO



“Mulungu sanatsiye opanda zida, koma pali zinthu zimene Akhristu onse ayenera kuchita kuti ateteze ndi kukulitsa unansi wao ndi Mulungu.”

Pamene munthu wapulumutsidwa nafulatira zinthu za dziko lapansi, posakhalitsa zenizeni za moyo watsopano zimayamba kukhazikika pa otembenuka mtima uja. Mdaniyo adzayesa kumupanikiza Mkhristu watsopanoyo ndi mafunso, kukaikira ndi mantha. Pali makiyi a choonadi amene akagwiritsidwa ntchito ndi kutsatiridwa, adzathandiza wotembenuka kumeneyo kukhala wokhulupirika ndi kukula m'zinthu za Mulungu.

Simuli nokha

Pali zoonadi za m'Baibulo, mfunso zothandiza, ndi malangizo zimene zili ofunika kwambiri kuti Mkhristu watsopanoyo apambane. Chipulumutso ndi chochitika chodabwitsa, koma monga ndi chinthu chilichonse chabwino, pali kuyesetsa ndi ntchito yofunika pofuna kusunga moyo watsopano mwa Khristu. Mulungu sanatsiye opanda zida, koma pali zinthu zimene Akhristu onse ayenera kuchita kuti ateteze ndi kukulitsa unansi wao ndi Mulungu. Opolumutsidwa kumene samayitanidwa ku moyo wachiyero popanda thandizo la Mulungu. Ngati mungadzipezere nokha makiyi anzeru awa omwe akhala akugwiritsidwa ntchito ndi ana a Mulungu, tsogolo lanu lidzakhalala lowala, ndipo mudzatha kukhala ndi moyo wodlalitsika mwa Khristu. “Momwemo monga munalandira Khristu Yesu Ambuye, yendani mwa Iye: Ozika mizu ndi omangidwa mwa Iye, ndi okhazikika m'chikhulupiriro, monga munaphunzitsidwa, ndi kukuruka m'chiyamiko” (Akolose 2:6-7).

Sungani cholinga chanu ndi chisankho chanu

Mtima ndi chikhumbo zomwe zinakokera wochimwa kwa Khristu kuti apulumutsidwe zikuyenera kukhazikika ndi cholinga chotsatira Yesu. Dziko lidzayesa kukokera wotembenuka kuti abwerere, ndipo mayesero akale nthawi zambiri amakokera thupi ku zakale. Kiyi wofunika kwambiri pofuna kupambana tsiku ndi tsiku ndiye “kufunafuna zakumwamba” ndipo “Lingalirani zakumwamba osati za padziko ai” (Akolose 3:1-2). Chipulumutso nchaumulungu, koma Mkhristu ayenera kupanga chisankho akudziwa chimene akupanga: “Sindidzabwerera ku dziko

lapansi.” Paulo anakumbutsa otembenuka mtima ku Korinto za chifuno chao choyambirira: “Pakuti, taonani, ichi chomwe, chakuti mudamvetsedwa chisoni cha kwa Mulungu, khama lalikulu lanji chidalichita mwa inu, komanso chodzikonza, komanso mkwiyo, komanso mantha, komanso kukhumbitsa komanso changu, komanso kubwezera chilango! M'zonse munadzitsimikizira nokha kuti muli oyera mtima m'menemo” (2 Akorinto 7:11). Kusamalitsa kwa cholinga kumeneku kudzalimbikitsa Akhristu pamene akumana ndi zotsutsana nazo komanso mayesero.

Imani m'chikhulupiriro, osati m'zoimvaimva

Mutatha kupempherera chipulumutso, dzuwa lidzalowa, tsiku lina lidzayamba, ndipo zomverera za mthupi ndi chisangalalo cha kukhudzika kawirikawiri sizimamveka mwamphamvu motero. Otembenuka mtima ambiri amakayikira ngati anapulumutsidwa pamene zomverera zamthupi zazilala. Kiyi amene tigwiritse ntchito pa nthawi ino ndi wa chikhulupiriro, “Pakuti tiyendayenda mwa chikhulupiriro si mwa chionekedwe” (2 Akorinto 5:7). Malingaliro ndi abwino ndi odabwitsa, koma chipulumutso sichikhudzana ndi zomverera za mthupi. Zomverera zimabwera ndi kupita, pamene mphatso ya Mulungu ndi yotsimikizika. “Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chili mphatso ya Mulungu” (Aefeso 2:8). Khulupirirani zabwino za mwazi wa Khristu wokhetsedwa m'malo mwanu, ndipo musadalire zokumvaimva za mthupi mwanu kapena ntchito zanu. Ngakhale kukayikira ndi malingaliro, palibe “Chifukwa chake tsopano

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)



iwu akukhala mwa Khristu Yesu alibe kutsutsidwa” (Aroma 8:1). Mdierekezi akamatsutsa chipulumutso chanu, ndi nthawi yabwino kudzifunsa kuti: “Kodi ndabwerera ku uchimo? Kodi ndikufunabe kutumikira Yehova?” Ngati muli omasuka ku uchimo ndipo mukufunabe kutumikira Ambuye, sangalalani ndi mphatso ya Mulungu ndipo mupirikitse mdierekezi ndi zoneneza zake.

“Pamene tikuyandikira kwa Yesu, timakhala ngati Iye. Timabala zipatso osati chifukwa cha kufunitsitsa kwathu koma chifukwa cholumikizidwa mu ubale ndi Khristu.”

Dziwani Yesu

Moyo wachikhristu suyenera kufotokozedwa ndi malamulo koma mwa ubale ndi Mulungu. Akhristu nthawi zambiri amavutika kuti ayese kukhala ngati Khristu, komabe amangoperewera. Kuyesetsa kumeneko kukanakhala kwabwino ngati kungatithandize kuti tiyandikire kwa Mulungu. Yesu ananena pa Yohane 15:4-5 kuti: “Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa inu. Monga nthambi siingathe kubala chipatso pa yokha, ngati siikhala mwampesa; motere mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine. Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake: wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu.” Pamene tikuyandikira kwa Yesu, timakhala ngati Iye. Timabala zipatso osati chifukwa cha kufunitsitsa kwathu koma chifukwa cholumikizidwa mu ubale ndi Khristu. Ubale umenewo sukhazikika pa mantha koma pa kukonda Mulungu ndi mtima wathu wonse.

Yendani tsiku lililonse mokondweretsa Mulungu

Monga ana amene timakonda Atate wathu, tidzayesetsa kumukondweretsa ndi kumumvera. Yesu anati, “Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga” (Yohane 14:15). Chinsinsi cha chipambano ndicho kuyenda tsiku ndi tsiku kuti tikondweretse Mulungu. Izi zikutanthauza kukhala oyera ndi oyera chifukwa ndi chifuniro cha Atate. Pamene mafunso abuka ponena za chochita, tsatirani uphungu wa mtumwi Paulo wakuti: “Chifukwa chake mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale muchita kanthu kena, chitani zonse ku ulemerero wa Mulungu” (1 Akorinto 10:31). Choncho, tsatirani malangizo a mtumwi Paulo akuti: Tikamachita zinthu zimene sizilemekeza Mulungu, kachitidwe kathu mmene timamudziwira Mulungu kamayamba kuonongeka.

Gwiritsani ntchito kiyi wa chisomo

Mulungu wapatsa ana ake makiyi odabwitsa akuti agwiritse ntchito pa nthawi ya mavuto, mayeso ndi mayesero. Iwo ndiwo makiyi a chisomo. Kukondera kwa Mulungu kuli

thandizo kwa ife pamene tili osayenerera chifundo ndi mphamvu yake. Petro anatiphunzitsa kuti “kulani m’chisomo” (2 Petro 3:18). Funafunani thandizo la Mulungu ndi kukula m’kukond eredwa kwake. Tikamavutika, si nthawi yoti tidzitalikitse kwa Mulungu. Yakwana nthawi yoti tikhale osatetezeka ndiponso “tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa.” (Ahebri 4:16). Musataye mtima mukakhala kuti ndinu wofooka komanso wosakwanira. “Chisomo changa chikukwanira” (2 Akorinto 12:9) ndipo mphamvu yake idzaonekera mu kufooka kwanu ngati mudalira mwa Iye. Ndi mdalitso wake kukhala ndi gwero la chisomo ili lomwe silimauma.

Chepetsani mayesero

Malinga ngati tili padzikoli, tidzakhala ndi mayesero. Palibe chidziwitso cha chipulumutso chimene chidzachotsa zipsinjo zonse ndi zotikokera pansu za uchimo ndi thupi. Komabe, sitiyounera kugonja ku ziyeso zimenezo. Ndikofunika kupanga zisankho kuti muchepetse mayesero a moyo. Yesu anauza ophunzira ake pa Mateyu 26:41 kuti: “Chezerani ndi kupemphera, kuti mungalowe m’kuyesedwa: mzimutu uli wakufuna, koma thupi lili lolefuka.” Tisangopemphera kokha ndi kuzindikira mayesero athu, komanso tiyenera kuwathawa. Sitiyounera kusewera ndi mayesero, “Koma valani inu Ambuye Yesu Khristu, ndipo musaganizire za thupi kuchita zofuna zake” (Aroma 13:14). Dzitalikitseni nokha kwa anthu ndi zinthu zokopa zomwe zimatsegula chitseko cha mayesero m’moyo wanu. Sankhani kukhala ndi moyo wosamalitsa, ndipo chisomo cha Mulungu chidzakuthandizani kupirira mayesero. Koma mukakhala mosasamala ndi kuchita zinthu zimene zingapangitse kuti muchimwe, mudzapeza kuti chisomo cha Mulungu sichigwira ntchito, chifukwa chilibenso ntchito ndipo chili chopanda popeza mwachita kusankha.

Khalanibe ndi chikumbumtima choyera

Munthu akapulumsidwa koyamba, ayenera kubwezera amene adamulakwira, monga momwe Zakeyu adachitira pa Luka 19:8-9. Komabe, Akhristu ayenera kuyesetsa kuchita zinthu tsiku ndi tsiku monga mmene Paulo. Iye anayesetsa kuti moyo wake ukhale wopanda chifukwa pamaso pa Mulungu ndi anthu. “M’menemonso ndidziyesera ndekha ndikhale nacho nthawi zonse chikumbumtima chosanditsutsa cha kwa Mulungu ndi kwa anthu” (Machitidwe 24:16). Pamene mwalakwitsa ndipo mukulephera kufika pa chidzalo cha

chipatso cha Mzimu, mufulumire kudzichepetsa ndi kuvomereza chosowa chanu. Izi zimalimbikitsa kukula kwa uzimu pamene mukusunga umboni wopanda banga.

Phunzirani Baibulo

Kuwerenga Baibulo tsiku lililonse ndi kofunika kwambiri kuti munthu akule mwauzimu. “Lirani monga makanda alero mkaka woyenera, wopanda chinyengo, kuti mukakule nao kufikira chipulumutso” (1 Petro 2:2). Kodi tikhoza kudziwa bwanji mmene tingakondweretse Ambuye ngati sitikhala ndi nthawi yowerenga mau ake? Baibulo ndi Mau a Mulungu ndipo linaperekedwa pa “chiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m’chilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iliyonse yabwino” (2 Timoteo 3:16-17). Pali mau ambiri m’dziko lachipembedzo, ndipo m’pofunika kuphunzira gwero lenileni la choonadi ndi kulingalirapo. Monga momwe Davide ananenera pa Salmo 119:105, “Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga.”

Lankhulani ndi Mulungu

Pemphero ndi imodzi mwa makiyi ofunika kwambiri pofuna kukhala ndi madalitso auzimu ndi chipambano. Kodi tiyenera kupemphera kangati? “Pempherani kosalekeza” (1 Atesalonika 5:17). Patulani nthawi yapadera yopemphera kwa Atate wanu wa Kumwamba. Choyamba chenicheni m’mawa pempherani musanakumane ndi mayesero a moyo. Pempherani musanagone usiku ndipo khalani ndi malingaliro ndi mtima woyankhulirana ndi Ambuye nthawi zonse. Mulungu ndiye bwenzi lathu, wonyamula zothodwetsa, wothandiza, wotonthoza ndi wotitsogolera. Tsekulani mtima wanu ndi kulankhulana momasuka ndi Mulungu. Mulungu amatikondweretsedwa ndi pemphero ndipo amatipatsa mwai wopemphera. “M’zonse ndi pemphero, ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu” (Afilipi 4:6). Pamene chidziwitso cha uzimu cha Mkhristu chikhala chofooka ndi chozilala, mudzapeza kuti nthawi zambiri moyo wa pemphero ukusowa.

Kuyanjana ndi okhulupirira ena

Kudzipatula mwauzimu kwachititsa kuti ana ambiri a Mulungu afe kuuzimu. Kuyanjana ndi oyera mtima ena ndikofunikira, ndipo ndikofunikira kuti otembenuka apeze malo oyanjana kumene choonadi chikuphunzitsidwa ndi kupezeka. Kungakhale bwino kukhala m’malo osaoneka bwino koma ndikumapeza ndalama zochepa pantchito pamene ukukhala paubale ndi oyera mtima sabata iliyonse kusiyana ndi kudzipatula nkumakhala wekha koma ndi kugonjetsedwa ndi zochitika za m’dziko. Izi zawachitikira anthu ambiri komanso mabanja achinyamata. Malangizo anaperekedwa pa mfundo imeneyi pa Ahebrei 10:25. “Osaleka kusunkhana kwathu pamodzi, monga amachita ena, komatu tidandaulirane, ndiko koposa monga momwe muona tsiku lilikuyandika.” Kodi moyo wanu ndi wofunika bwanji? Musanyalanyaze utumiki wanu ndi kulambira limodzi ndi anthu a Mulungu.

Nenani za umboni wanu

Chinsinsi china cha chigonjetso chazimu ndikugawana ndi ena za umboni wanu wa chipulumutso. Oyera mtima akale anagonjetsa mdierekezi “ndi mau a umboni wao”



(Chivumbulutso 12:11). Pamene tigawana ndi ena zomwe takumana nazo patokha, sikungokhala umboni ku dziko lapansi, komanso kumalimbitsa chikhulupiriro chathu ndikuthandizira kuthana ndi zoneneza za mdani. Zimatilimbitsa mwauzimu. Pakuti “Uthenga Wabwino sundichititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa” (Aroma 1:16). Pamene tigawana ndi ena zimene Mulungu watichitira ifeyo patokha, timathandizanso kukwaniritsa ntchito ya Khristu yakuti, “Mukani kudziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino” (Marko 16:15).

Gwirirani ntchito Mulungu

Mulungu sanatipulumutse kuti tikhale pansu ndi kudikira kubwera kwa Ambuye Yesu. Mu Ufumu wa Mulungu muli ntchito yoti tizigwira tonse. Anthu abwerera m’mbuyo chifukwa anakhala aulesi ndipo sanatanganidwa ndi kutumikira Yehova. Ndife “olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m’menemo.” (Aefeso 2:10). Pamene anthu a dziko lapansi akuwunjika chuma padziko lapansi, ana a Mulungu ayenera “kudziunjikira okha chuma m’Mwamba” (Mateyu 6:19-20). Timakhala olimba mu uzimu tikamatanganidwa ndi ntchito za Ambuye. Paulo anati: “popeza muli ofunitsitsa mpatso za Mzimu, funani kuti mukachuluke kukumangirira kwa Mpingo” (1 Akorinto 14:12). Tumikirani kwa anthu ena, ndipo mudzalimbikitsidwa muzochitika zanu zauzimu. Ngati mufuna kuona Mkhristu amene ali wofooka komanso ali pachiopsezo, yang’anani amene akukhala modzikonda kwa iye mwini ndipo sakugwira ntchito za ufumu wa Mulungu.

Nyimbo ina imati, “Wamphamvu kupulumutsa, wamphamvu kusunga.” Ntchito yoyambirira ya chipulumutso ndi yodabwitsa, koma chiri pafupifupi chozizwitsa chachikulu kukhalabe opulumutsidwa ndi okhulupirika kwa Ambuye. Yesetsani kuti muchite mwanzeru ndi kugwiritsa ntchito makiyi ali pamwambawa mwaubwino, ndipo mudzasangalala ndi madalitso ochuluka ndi chigonjetso mwa Khristu Yesu. ■



KODI MUKUDZIWA?

“Moyo umene uli pa guwa subweretsa chisangalalo m'magulu ena chifukwa timazindikira kuti anthu pafupifupi 95 mwa 100 aliwonse salowa mu mpingo. Makamaka, ambiri a iwo sadzabwereranso kachiwiri ku tchalichiko.” - Charles E. Hackett

Chipulumutso chili choposa kungovomera pamene waitanidwa ku guwa kapena kusankha kwakanthawi. Kuli kusintha kwa moyo pamene otembenuka mtima ayenera kutsatira Yesu tsiku ndi tsiku kuopera kuti dzina lao lingangokhala mu buku basi.



MULUNGU ADZAMALIZA ZIMENE WAYAMBA


Pokhulupirira pamene, kuti Iye amene anayamba mwa inu ntchito yabwino, adzaitiriza kufikira tsiku la Yesu Khristu. — Afilipi 1:6

Pamene munthu wochimwa abwera kwa Khristu ndi mtima wolapadi, Kumwamba kumakhala chisangalalo. Mulungu amaumbanso mtima wosweka, nayeretsa osalungama ndi kusanduliza wochimwa kukhala wolengedwa watsopano. Chimakhala chinthu chodabwitsa cha mtendere ndi chachimwemwe pamene wotembenuka akuyenda mu moyo watsopano.

Chochitika choyambachi chimakhala chiyambi chabe. Pali moyo wakuti munthuyo akhalemo ndipo mkhristu watsopanoyo posakhalitsa adzakumana ndi zenizeni zokhudza iye mwini, mayesero komanso zopweteka. Imeneyi si nthawi yoti akhumudwe kapena kuzisiya zinthu za Mulungu. Mkhristu akuyenera kulimba mtima ndi kukhala wotsimikiza kwathunthu, monga anachitira mtumwi Paulo, amene “wokhulupirira” kuti Mulungu amene anapulumutsa adzapitiriza kugwira ntchito ndi kupangitsa mwana wa Mulungu kuti apambane mpaka kubweranso kwa Yesu.

Mulungu sanatumize Mwana wake kuti adzatifere chifukwa cha machimo athu kuti agwire ntchito yochepa chabe. Iye watipatsa zonse zimene timazifuna kuti tipambane pa mavuto a moyo. Mulungu amadziwa zofooka zathu, zovuta zathu, ndi zizolowezi zathu. Iye amadziwa zonse zokhudza ife, ndipo tikhoza kupumula ndi chitsimikizo chakuti Mulungu ali wofunitsitsa ndipo akhoza kutumikira ku zosowa zathu kwathunthu. Iye adzatipatsa mphamvu kuti titsatire Yesu mokhulupirika ndi kuti tidzapezeke okonzeka kukumana naye mu mtendere pa chiweruzo.

Chipulumutso ndi dongosolo lokwanira, ndipo ntchito ya Mulungu si yachisawawa. Iye sadzasiya ntchito imene wayamba. Iye adzatifikitsa ku mapeto kupyolera mu ntchito yopitirira ya chisomo ndi ya Mzimu Woyera. Mulungu amadziwa bwino za umunthu wathu, ndipo anakonzeratu zinthu zauzimu zokwanira kuti tipambane. Palibe vuto kapena msautso umene uli waukulu kwa Mulungu. Ngakhale titakhala kuti tili ndi mphamvu zakuti tikhoza kuchoka pamaso pa Mulungu, Iye sadzatisiya kapena kutitaya pamene tikupitirizabe kukhala ndi cholinga chakuti timutsatire. Ngati simusiya kutumikira Mulungu, Iye sadzakusiyani. Iye adzamaliza zimene anayamba m'moyo wanu! ■



Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE